Tony Alamo Christian Ministries
Nkhani za M'makalata za Dziko Lonse Lapansi
Yerusalemu Watsopano Matchalitchi Dziko Lonse
Mbusa Tony Alamo Fuko La Chikhristu La Alamo Volume 17400




# ASILIKALI A NKHONDO YAPAMTUNDA NDI MLENGALENGA A MULUNGU (ALONDA)

### Yolembedwa ndi Tony Alamo



*Abusa Tony ndi Susan Alamo pa purogaramu ya kanema yadziko lonse* *chithunzi chinajambulidwa 1973*

M'nyamata wa mneneri Elisa analawilira kudzuka mmawa ndipo anawona khwimbi la asilikali ankhondo aku Siliya atazungulira mzinda umene Elisa ndi iye anali. Mwamantha, anati kwa Elisa, "Kalanga ine, mbuye wanga! tipange chiyani? [kapena kuti, tichoka bwanji m'mavuto amenewa tili ndi moyo? Kenako Elisa anamuuza m'nyamata wakeyo kuti,] Usaope: pakuti amene ali mbali yathu ndi wochuluka kuposa amene ali mbali yawo iwo. Elisa anapemphera [KWA MULUNGU], AMBUYE, Ndikupemphera kwa INU, tsegulani maso ake, kuti m'nyamatayu aone. Ndipo AMBUYE anatsegula maso a m'nyamatayo; ndipo anaona: ndipo, taonani, phiri linali lodzadza akavalo ndi magareta amoto atazungulira Elisa" (2 Mafumu 6:15-17).

Asilikali kapena atumiki a MULUNGU omwewo amene Elisa anafunsa MULUNGU kuti amuonetse wantchito wake ndi asilikali kapena atumiki a MULUNGU omwewo amene anagwetsa zipupa za Yeriko (Yoswa 6:20). Yoswa anakumana ndi KAPITAWO wa atumiki a MULUNGU ku Yeriko mu njira imeneyi: "Ndipo zinachitika, pamene Yoswa anali pafupi ndi Yeriko, kuti anatukula maso ake napenya, ndipo, taonani, panaima munthu pafupi naye ali ndi lupanga LAKE mmanja MWAKE: ndipo Yoswa anapita kwa IYE, ndipo anati kwa IYE, NDIWE wambali yathu, kapena ya adani athu? Ndipo IYE anati, AYI; KOMA NGATI KAPITAWO WA ATUMIKI A MULUNGU [YESU m'thupi la munthu] NDABWELA TSOPANO. Ndipo Yoswa anagwetsa nkhope yake pansi, ndikupembedza, ndipo anati kwa IYE, Akuti chiyani AMBUYE wanga kwa watchito WAKE? Ndipo KAPITAWO wa Atumiki wa AMBUYE anati kwa Yoswa, Vula nsapato kumapazi ako; pakuti malo waimapowo ndi OPATULIKA. Ndipo Yoswa anachita monga anamuuzira.

"Tsopano Yeriko anatsekedwa movuta chifukwa cha ana a Israyeli: Palibe anatuluka ndipo palibe analowa. [Zinali chonchi chifukwa anadziwa kuti MULUNGU anali ndi a Israyeli, ndiponso amadziwa kuti MULUNGU akanawaononga.] Ndipo AMBUYE anati kwa Yoswa, Ona, ndapeleka Yeriko m'manja mwako, ndi Mfumu pa iyo, Ndi amuna amphamvu olimba mtima. Ndipo mudzazungulira mzinda, ndi anthu ako ankhondo, ndikuyenda mozungulira mzinda kamodzi. Chomwecho mudzachita masiku asanu ndi limodzi [zonsezi kunali kuchotsa zosalongosoka kwa anthu oipitsitsa aku Yeriko chisanachitike chiwonongeko chawo chotheratu chenicheni.] ndipo ansembe asanu ndi awiri adzabweletsa malipenga asanu ndi awiri a nyanga za nkhosa zazimuna pa chombo: Ndipo tsiku la chisanu ndi chiwiri mudzazungulira mzinda kasanu ndi kawiri, ndipo ansembe adzaimba malipenga. Ndipo zidzachitika, kuti pamene adzaimbe mokweza kwambiri ndi nyanga za nkhosa zazimuna, ndipo pakumva kulira kwa lipenga, anthu onse adzakuwa ndimkuwo waukulu; ndipo makoma a Yeriko adzagwera pansi [izi zidzakwaniritsidwa ndi nkono wosawoneka wa otumikira AMBUYE] ndipo anthu adzakwenza kumwamba munthu aliyense molunjika pamaso pake.

"Ndipo Yoswa mwana wa Nun anaitana ansembe, nati kwa iwo, Tengani chombo cha chipangano, ndipo lolani ansembe asanu ndi awiri abwele ndi malipenga

*(Yapitirira patsamba 2)*

## ASILIKALI A NKHONDO YAPAMTUNDA NDI MLENGALENGA A MULUNGU
### (ALONDA)

*(Yachokera patsamba 1)*

asanu ndi awiri pamaso pa Chombo cha AMBUYE. Ndipo anati kwa anthu, Pitani, ndikuzungulira mzinda, ndipo kwa iye yense wazida mukawapeleke pamaso pa chombo cha AMBUYE. Ndipo zinachitika, pamene Yoswa anayankhula kwa anthu, kuti amsembe asanu ndi awiri [Ayuda] okhala ndi malipenga asanu ndi awiri a nyanga za nkhosa zazimuna anayenda pamaso pa AMBUYE, ndikuyimba malipenga: ndipo chombo chachipangano cha AMBUYE chinawatsata. Ndipo amuna okhala ndi zida anapita pamaso pa ansembe amene anaimba malipenga, ndipo otsatira anabwera pambuyo pa chombo, ansembe kupitilirabe, ndikuimba malipenga. Ndipo Yoswa analamula anthu, nati, Simudzakuwa, ngakhalenso kupanga phokoso lililonse ndi mawu anu, ndipo palibe liwu lililonse lidzatuluke kuchoka mkamwa mwanu, mpaka tsiku lomwe ndidzakuuzeni kuti kuwani; ndipamene mudzakuwe.

"Tsopano chombo cha AMBUYE chinayenda mzinda wonse, kuzungulira mzindawu kamodzi: ndipo anabwera ku Msasa, ndikugona mu Msasa. Ndipo Yoswa analawilira kudzuka m'mawa, ndipo ansembe anatenga chombo cha AMBUYE. Ansembe asanu ndi awiri omwe anatenga malipenga a nyanga za nkhosa zazimuna pamaso pa chombo cha AMBUYE anapitilirabe, ndikuimba malipenga: ndipo amuna okhala ndi zina anapita pamaso pawo: koma otsatira anabwera pambuyo pa chombo cha AMBUYE, ansembe kupitilirabe, ndikuimba malipenga. Ndipo tsiku lachiwiri anayenda mzinda wonse kamodzi, ndikubwelera ku Msasa: kotero anapanga masiku asanu ndi limodzi.

"Ndipo zinachitika pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, kuti anadzuka molawira chakum'bandakucha, ndikuzungulira mzinda wonse mwachidzolowezi kasanu ndi kawiri: patsiku lokhali anazungulira mzinda kasanu ndi katatu. Ndipo zinachitika kachisanu ndi chiwiri, pamene ansembe anayimba malipenga, yoswa ananena kwa anthu, kuwani; pakuti AMBUYE wakupatsani mzinda. Ndipo mzindawu udzatembeleredwa, ngakhale iwo, ndi zonse zokhala mmenemo, kwa AMBUYE: Rehabu mkazi wachiwerewere ndi yekhayo adzakhalemo, iye ndi anthu onse akukhala naye limodzi mnyumba, chifukwa anabisa atumiki omwe tinawatumiza. Ndipo inu, mu nzeru zilizonse dzitalikitseni ndi chinthu chotembeleredwa, kupanda apo mudzadzipanga nokha kukhala otembeleredwa, mukatenga chinthu chotembereredwa, ndikupanga msasa wa Israeli kukhala themberero, ndikuwusowetsa mtendere. Koma zonse Siliva, ndi Golide, ndi ziwiya za brasi ndi aironi, ndizopatulika kwa AMBUYE: Zidzabwera munkhokwe yosunga chuma cha AMBUYE.

"Anthu anakuwa pamene ansembe anayimba malipenga: ndipo zinachitika, pamene anthu anamva kulira kwa malipenga, ndipo anthu anakuwa ndi mkuwo waukulu, mwakuti khoma linagwelatu lonse pansi [izi zinakwaniritsidwa ndi atumiki a AMBUYE ndi KAPITAWO wa atumiki a AMBUYE], mwakuti anthu analowa mumzindawo, munthu aliyense patsogolo pamzake, ndipo anatenga mzinda" (Yoswa 5:13-6:20).

Mubuku la Enoki, Mneneri Enoki alosera za alonda. Alondawa ndi angelo a MULUNGU, ndipo ndi atumiki a Kumwamba a AMBUYE. Nthawi zina amatchulidwa kuti angelo osamala a anthu olungama a MULUNGU pano pa dziko lapansi.

Pali angelo oyipa, ndipo palinso angelo abwino. Chibvumbulutso 12:4 amanena kuti ⅓ mwa angelowa—oipawa—anathamangitsidwa kuchoka kumwamba pamodzi ndi mtsogoleri wawo, satana mwiniwake (Luka 10:18). Koma kumbukilani, ⅔ ya angelowa—abwinowa—anatsalira kugwira ntchito za MULUNGU. Angelo oipawa, ⅓, sioyipa kokha ayi, koma ochita za uchimo kwambiri.

Chibvumbulutso 12:3 amati "ndipo kunaoneka chodabwitsa china kumwamba; ndipo taonani chirombo chofiira [m'dyelekezi] cha mitu isanu ndi iwiri…" "Mitu isanu ndi iwiri ndi mapiri asanu ndi awiri [aku Rome, Italy], omwe mzimayi amakhalapo" (Chibvumbulutso 17:9). Mzimayiyu ndi mneneri wonyenga, tchalitchi chachinyengo, chipembedzo chaupandu, mutu wa chirombo umene uli Vatican, Roma Katolika, ogonana amuna kapena akazi okhaokha, tchalitchi chochita zachiwerewere ndi ana.

Chibvumbulutso 12:3 anapitilira kunena kuti mitu isanu ndi iwiri imeneyi ili ndi nyanga khumi. Nyanga khumi zimenezi zikuimira maiko khumi aku Ulaya omwe amapereka mphanvu zawo ku Vatican yaku Rome (U.N., New World Order) pa kanthawi kochepa (Greece ndi lomalizira), lomwe lagwirizana ndi New World Order ya Satana, kapena dziko la boma limodzi. "…Ndipo zisoti zisanu ndi ziwiri pamutu pake [zisotizi zikuyimira New World Order ya m'dyelekezi kulamulira mongoyembekezera pa makontinenti asanu ndi awiri, kapena m'mawu ena, dziko lonse lapansi]."[1]

"Ndipo mchila wake unakopa gawo lachitatu la nyenyezi za Kumwamba [Nyenyezi ndi angelo oipa.[2] Chibvumbulutso 1:20 amati nyenyezi ndi zizindikilo za angelo], ndipo [chirombo, Satana] anaponya [⅓ ya angelo oipa ndiaumdyelekezi] kudziko lapansi: ndipo chirombo [mdyelekezi] anaima pamaso pa mkazi [yemwe ali ndi nyenyezi khumi ndi ziwiri muchisoti chake. Uyu (mkazi) ndi Mkwatibwi wa KHRISTU, Yerusalemu Watsopano, limene lili THUPI la KHRISTU lenileni pano pa dziko la pansi, Israeli owona, amene ali a Khristu, osati a Katolika, omwe amachokela ku anthu osankhidwa enieni a MULUNGU, Ayuda. Tsopano MULUNGU watsegula chipulumutso kwa anthu amitundu yonse omwe adzavomeleze KHRISTU kukhala chipulumutso chawo]" (Chibvumbulutso 12:4).

Chibvumbulutso 12:4 amati mkazi ameneyu (THUPI la KHRISTU) ndiwokonzeka kubereka mwana wake, amene ali KHRISTU. Ichi ndi chikumbutso cha nthawi yomwe satana, kudzera mwa Mfumu Herodi ndi asilikali ake, anaima pamaso pa Israeli kufuna kuononga KHRISTU pa tsiku LAKE lobadwa ndi/kapena kudutsa zaka ziwiri,[3] chifukwa KHRISTU anali ndipo adakali MFUMU wa mafumu ndi AMBUYE wa ambuye, MPULUMUTSI wa dziko lapansi, IYE amene adzaononge ntchito za satana populumutsa mizimu ya onse adzamulandire IYE kukhala Mpulumutsi wao komanso olamulira.[4] Akolose 2:15 amati KHRISTU, "atasokoneza ulamuliro wa chifumu ndi mphamvu…anawayalutsa poyelayela, powagonjetsa."

Awa ndimasiku omaliza.[5] Dziko ladzadza ndi asilikali a MULUNGU, ndipo m'mlengalenga mwadzadza ndi

**1** Dan. 2:40, 7:19-25, Chiv. 13:2-8, 14:8, chap. 17, 18:2-24 **2** Yes. 14:12-17, Mat. 25:41, Luka 10:18, 2 Pet. 2:4, Yud 6, Chiv. 12:3-4, 7-9 **3** Mat. 2:1-18 **4** Dan. 7:13-14, 1 Tim. 6:14-16, Aheb. 2:14-15, 1 Yoh 3:8, 4:14-15, Chiv. 17:14, 19:16 **5** Mat. chap. 24

asilikali a Mulungu am'mlengalenga. Amenewa ndi maUFO omwe anthu mamiliyoni awawona pa dziko lonse lapansi. Chifukwa anthu a dziko lapansi amanyozera za MAU a MULUNGU, amakhulupilira kuti maUFO amenewa ndi alendo ochokera kumayiko ena.Tikadziwa Baibulo, tadziwanso mmene anthu a dziko lapansi anyengedwela, chifukwa "mbale zowulukazi," zimene zimatchulidwa kuti maUFO, sizochokera kumapulaneti ena. Ndi "alonda," angelo a MULUNGU, kuyendera dziko lapansi KHRISTU asanabwerenso padziko lapansi. Alonda akukonzekera Chiweruzo.

Chivumbulutso 16:1 imati, "ndipo ndinamva mawu amphamvu kuchokera mutchalitchi kupita kwa angelo, Pitani njira zanu, ndipo mukasinthule zikho za mkwiyo wa MULUNGU ku dziko lapansi." Danieli 4:13, "Olondera [m'ngelo] pamodzi ndi Iye Wakuyera anatsika kuchoka Kumwamba" kubweretsa chiweruzo cha MULUNGU pa Mfumu yamwano Nebuchadnezzar, yemwe ananena pa Danieli 4:30, "Kodi si Babulo opambanayu, yemwe ndamangira nyumba yachifumu ndi mphamvu yanga, [mmalo mwa mphamvu ya MULUNGU], ndipo ulemu wa ufumu wanga [mmalo mwa ulemu wa MULUNGU]?"

Ichi ndi chiweruzo cha Mulungu chimene chinapelekedwa kwa mlonda kuti akachite mwakutsutsa Nebuchadnezzar. "Pamene liwu [lidakali] mkamwa mwa mfumu [yamwano], panagwa liwu lochoka kumwamba, lakuti, O mfumu Nebuchadnezzar, kwa inu mwayankhulidwa; ufumu wachoka kwa inu. Ndipo iwo [alonda] adzachotsa iwe pakati pa anthu, ndipo pokhala pako padzakhala ndi chirombo cha m'munda: adzapanga iwe kudya udzu ngati ng'ombe, ndipo nyengo zisanu ndi ziwiri zidzakudutsa iwe, mpaka udzadziwe kuti WAM'MWAMBA MWAMBA amalamulira ufumu wa anthu, ndipo amapereka kwa aliyense mwachifuniro CHAKE. Ola lomwelo zinakwaniritsidwa kwa Nebuchadnezzar: ndipo anachotsedwa pakati pa anthu, ndipo anadya udzu ngati ng'ombe, ndipo thupi lake linali lonyowa ndi mame akumwamba, mpaka tsitsi lake linakula ngati nthenga za chiomba nkhanga, ndipo zikhadabo zake ngati zikhadabo za mbalame" (Danieli 4:31-33).

Mu Yeremiya 4:16, MULUNGU anauza Yeremiya, "Nena kwa mitundu; taonani, lembani zotsutsana ndi Yerusalemu, kuti alonda amachokera kudziko lakutali, ndikupereka mawu awo otsatsuna ndi mizinda yamu Yudea." Pakhala pali mkwiyo waukulu wotsutsana ndi mizinda yaku Yudea. Ndi choncho chifukwa chakuti akukanabe YESU kukhala MESIYA mpaka lero.

Muchifundo cha MULUNGU, IYE akulora aliyense kuti athe kuona mahandiredi a maulosi a nthawi zotsiriza, zizindikiro, ndi zodabwitsa monga alonda, angelo a MULUNGU, kuyendera dziko muzotchedwa "mbale zowuluka" isanafike nthawi yoti ilo (dziko) liwonongedwe. Bukhu la Yoweli linalosera izi,[6] ngatinso wachitira Mtumwi Petulo mubukhu la Machitidwe: "Ndipo zidzachitika m'masiku otsiriza, atero MULUNGU, ndidzakhuthula MZIMU WANGA pa minofu yonse: ndipo ana anu amuna ndi akazi adzalosera, ndipo anyamata anu adzawona maso mphenya, ndipo achikulire anu adzalota maloto: Ndipo pa antchito ANGA ndipa antchito ANGA akazi ndidzakhuthula m'masiku amenewo MZIMU WANGA; ndipo adzalosera: Ndipo ndidzachita zodabwitsa m'mwamba, ndi zizindikiro m'dziko lapansi; mwazi, ndi moto, ndi mthunzi wa utsi: Dzuwa lidzasandulika mdima, ndipo mwezi kukhala mwazi, lisanafike tsiku lalikulu lozindikirika lobwera AMBUYE: Ndipo zidzachitika, kuti aliyense woyitanira pa dzina la AMBUYE adzapulumutsidwa" (Machitidwe 2:17-21).

Ndikhulupilira kuti pafupifupi aliyense padziko pano akudziwa za zooneka mamiliyoni zomwe zimatchedwa ma UFO (zinthu zowuluka zosadziwika), koma izo sizili ma UFO ayi. Ndi alonda kapena angelo a MULUNGU kuyendera dziko munthawi iyi yomaliza chisanafike chigamulo cha MULUNGU, kutha kwa dziko, kutha kwa nthawi.

Alonda, amene ali, angelo Kumwamba, ndipo ife amene tili a Khristu (osati a Katolika), ndife pachibale pakuti MULUNGU anatilenga tonse. MULUNGU analenga angelo, ndipo MULUNGU anatilenga ife. Pali anthu abwino, ndipo pali anthu oipa, chifukwa ndi ochepa mwa ife timasunga malamulo a MULUNGU.[7] Yohane woyamba 2:3-4: "Ndipo pakutero tidziwa kuti timudziwa IYE, ngati tisunga malamulo AKE. Yense wakunena, ndim'dziwa IYE, koma osasunga malamulo AKE, ndionama, ndiponso chilungamo mulibe mwa iye."

Anthu ena amati amamukonda MULUNGU. Komabe, m'moyo wawo watsiku ndi tsiku, samayankha kuyitana kwa MULUNGU, koma mmalo mwake amanyozera mawu AKE. Ena amanena luti amakonda AMBUYE pokhapo pamene asangalala. Mwachitsanzo, akafuna kuwonela filimu, kapena kuwonela pologaramu pa kanema, za masewero, kapena zochitika za zoimbaimba, maganizo ena mwa iwo amawaletsa kuti asapite, koma amapitabe. Amadziwa kuti asachite machimo akulu, koma salabadira pa zomwe amaganiza kuti ndizazing'ono. Pa nthawi yopemphera m'magulu, amatha ngakhale kupereka umboni kuti agwidwa ndi MZIMU wa AMBUYE. Pali a Khristu ambiri onamizira angati amenewa. Apatu, kukonda AMBUYE munjira imeneyi ndi kopanda pache.[8]

*(Yapitirira patsamba 4)*

---

**6** Yow 2:28-32

**7** Mat. 7:13-14, 21-23, Luka 13:23-30 **8** Mat. 7:21-23, chap. 25

## Kuchokera ku Mapemphero Athu a Maola 24 ndi Ndondomeko za Nthawi

M'busa Wilimena Thomas (ku Lauderdale Lake, FL) analandila katundu wake. Amayi onse mugulu lawo lophunzira Baibulo anakhala pansi ndi kuwerenga "Asilikali Apamtunda ndi Mlengalenga a Mulungu." Iye anati anaphunzira zambiri kuchoka kuzina mwa zolembedwa kusiyana ndi mmene akhala akumvera kuchoka kwa azibusa ena kwa zaka (sanamve kuchoka kwa m'modzi mwa iwo kwakanthawi). Onse anasangalala ndi zolembedwazo ndipo akumvera ma CD. Iwo anati palibe yemwe amatha kulongosola bwino zinthu ngati momwe Tony amachitira. Iye anati chonde mupitirize kutumiza ma CD ndi mabuku. Iwo akufuna ife tidziwe kuti amasonkhana komanso amakhala ndi mkumano wamapemphero ndipo akupemphelera Tony ndi tchalitchi. Anapempha kuti azitumiziridwa mabuku ndi ma CD atsopano. Iye anapemphanso kuti tchalitchi chizipemphelera zidzukulu zake zitatu zolowelera zomwe zakhala zikuchititsidwa umboni kwa zaka.

## ASILIKALI A NKHONDO YAPAMTUNDA NDI MLENGALENGA A MULUNGU (ALONDA)

*(Yachokera patsamba 3)*

M'chemwali wina akhonza kukhala wa chidwi paza AMBUYE mwakuti kuphatikiza azichimwene khumi sangafanane naye. Akamakamba kokhudza kukonda AMBUYE, womvetsera wonse atha kukhudzidwa mpaka misonzi. Modabwitsa, komabe m'chemwaliyu akapsya mtima, palibe yemwe amatha kumuletsa. Umoyo wachilengedwe ndi umoyo wachinyengo (umoyo womwe suli wau MULUNGU). Tsiku lina, zonse zachilengedwe zidzanyenyedwa zidutswazidutswa. Tikuyenera kukhudzidwa ndi AMBUYE m'chowonadi kuwonetsetsa bwinobwino kuti chidwi chathu, kunamizira kwathu kapena kufunitsitsa konama, chikondi chathu chabodza pa AMBUYE ndi zintchito zathu zabodza kwa AMBUYE, ndizachilengedwe ndipo zosowekera mphamvu yau MULUNGU, sizenizeni. Posatengera kuchuluka kwa mphipi zamakoma azitsulo omwe tili nawo, ndi pakusatengera zakuti kaya chipata chakunja, chipata chapakati, kapena chipata chamkati, zonsezi ziyenera kutsegulidwa, chimodzichimodzi kwa AMBUYE, molingana ndi mmene MZIMU ulili. Kenako tidzazindikira kuti mmalongosoledwe achidwi ndikufunitsitsa kwathu, sitingamuone AMBUYE MWINIWAKE, pokhapokha ngati tasunthidwa ndi AMBUYE mpaka kufika poti ATHA kudzitulutsa mchowonadi kuchoka pakati pathu tidzakolora zipatso zambiri, ngati zanenedwa mu Yohane 15:2. Chipatso mumtengo chimachokera mu MOYO wa mkati mommo.

Tsopano, anthu omwe ali abale angelo oipa ndi anthu oipa. Koma kumbukirani, pali angelo auMULUNGU ambiri kuposa angelo aumdyerekezi. Elisa anawonetsa wantchito wake izi pamene asilikali aku Siliya anawazungulira iwo. Elisa anapempha kwa AMBUYE kutsegula maso a wantchito wake kuti wantchito wake athe kuwona kuti kunali ambiri ndi iye pamodzi ndi Elisa kuposa mmene analili asiliya. Atatero, "taonani, phiri linadzadza ndi akavalo ndiponso magareta amoto [atumiki AMBUYE] mozungulira Elisa [ndi wantchito wake]," ngati mmene zilili pano lero atumiki aufumu wa MULUNGU ndi alonda kutizungulira ndikutiteteza ife, kuona chilichonse chimene aliyense akuyankhula ndi chimene akuchita pano pa dziko. Zimenezi zikuchitika kudzera mwa alonda a MULUNGU paliponse kumwamba pambale zowuluka komanso pa alonda padziko—asilikali ankhondo apamtunda ndi mlengalenga a MULUNGU.[9]

Nthawi yakwana pano padziko kwa aliyense kulapa machimo ake ndikufuna MULUNGU ndi mtima, mzimu, maganizo, ndi mphamvu zawo zonse, limene lili lamulo loyamba ndi lofunikira kwambiri.[10] Pompano thambo lakumwamba lidzakutidwa ndi chizindikiro cha MWANA wa MUNTHU. Pali malemba ambiri amene amalongosola za nyengo imeneyi. Limodzi ndilo likuchokera ku Mateyu mutu 24. Lina ndilomwe likuchokera mutu wachiwiri wa Yesaya. Ndiponso lina likuchokera ku Chivumbulutso mutu 6.

Mateyu 24:30-51 imati, "Ndipo kudzaoneka chizindikiro cha MWANA wa MUNTHU kumwamba: ndipo mitundu yonse yadziko lapansi idzagwidwa ndi chisoni, ndipo adzaona MWANA wa MUNTHU akutuluka kuchoka kuthambo lakumwamba ndi mphamvu ndi ulemelero waukulu. Ndipo iye adzatumiza AKE [atumiki a AMBUYE, alonda], ndiphokoso lokweza lalipenga, ndipo adzasonkhanitsa pamodzi osankhika AKE kuchoka kumphepo zinayi, zochoka mbali ina kumapeto kwakumwamba kufikira mbali ina. Tsopano phunzirani za fanizo la mtengo wamkuyu; pamene nthambi yake ikali yanthete, ndipo ikutulutsa masamba, umadziwa kuti nyengo yotentha ili pafupi: chimodzimodzi, mukaona zinthu zimenezi, dziwani kuti yayandikira, ngakhale pazitseko. Zoonadi ndinena kwa inu, m'bado umenewu sudzadutsa, pokhapokha zinthu izi zitakwanilitsidwa. Kumwamba ndi dziko lapansi zidzatha, koma MAWU ANGA sadzatha… monga ngati mmene nthawi ya Nowa inalili,

**9** 2 Mbiri 16:9, Zak. 1:7-11, 4:10, 6:1-7, Chiv. 7:1-3 **10** Detro. 4:29, 6:5, 10:12-13, 11:13-14, 13:3-4, 16, 20, 26:16, 30:6, Yos. 22:5, Mat. 22:37-40, Mariko 12:29-31, Luka 10:27

## Peru

*(Zomasulidwa kuchoka muSpanish)*

Mulungu akudalitseni, m'bale, ndi utumiki wa Tony Alamo,

Ndikukudziwitsani kuti mwa ulemelero wa Mulungu, tsopano tili ndi tchalitchi chatsopano. Chili maola atatu kuchoka ku Sullana, kufupi ndi Piura, kumalo otchedwa Sechura, kumene kuli abale ndi alongo akuluakulu 23 ndi ana 33. Tinapita kukagwira ntchito, yogawa mabuku anu nyumba ndi nyumba ndipo ambiri amafunabe kuti aziphunzitsidwa. Dzulo tinakumananso ndipo abale ambiri anabwera. Analandira Ambuye ndipo tizikumana katatu pasabata. Ulemelero ukhale kwa Ambuye. Yesu akubwera posachedwa.

Andres Chiroque Silva
Tony Alamo Ministries
Sullana, Peru

## Kenya

Okondedwa M'busa Tony Alamo,

Landirani moni m'dzina la mphamvu loposa mayina ena onse, la Mbuye ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu. Ndine okondwa kukudziwitsani kuti zoonadi tikutenga Mzinda wathu ndi mabuku a Alamo omwe mukutitumizira. Tikufikira aliyense wopulumutsidwa ngakhalenso osapulumitsidwa, ndipo mwezi watha taona anthu akupulumutsidwa okwana khumi ndi mphambu zisanu (15), ndipo anthu amenewa tili nawo limodzi mu mpingo. Talandiranso katundu amene munatumiza pa 21 Disembala. Tikufuna kukuthokozani pamene tikupemphaso mabuku ndi mabaibulo enanso chifukwa anthu mambiri akuwafuna.

Mulungu akudalitseni pamene tikupitirira kupemphera kuti Mulungu alowelerepo pa nkhani ya M'busa wathu, chifukwa ndikudziwa kuti kudzera m'mapemphero china chilichonse ndi chotheka.

Ine wanu mu utumiki Wake,
M'busa Dalmas Munoko — Bungoma, Kenya



**MAUTUMIKI A ALAMO PA INTANETI**
**www.alamoministries.com**

ndimomwenso zidzakhalile panthawi yakubwera kwa MWANA wa MUNTHU. Pakuti munthawiyo hisanafike chigumula anali kudyelera ndi kumwelera, kukwatira ndi kukwatiwa, kufikira tsiku lomwe Nowa analowa muchombo. Ndipo sankadziwa mpaka chigumula chitafika, ndikukokolora onse; ndimmene kubwera kwa MWANA wa MUNTHU kudzakhalire… Choncho samalani: poti simudziwa nthawi imene AMBUYE adzafike. Koma dziwani ichi, ngati mwini nyumba akanadziwa nthawi yomwe wakuba adzafike, akanadziwa tcheru, ndipo sakanalora kuti nyumba yake ithyoledwe. Choncho nanu khalani okonzeka: poti nthawi yomwe inu simukuyembekezera ndiyomwe MWANA wa MUNTHU adzafike. Ndani tsopano mwa inu amene ali wantchito wokhulupilika ndiponso wanzeru, yemwe mbuye wake wamupanga kukhala woyang'anira katundu wamnyumba, kuwapatsa nyama m'nyengo yoyenelera? Odala ndi wantchito amene, pamene mbuye wake adzafike adzampeza akuchita mwakuyenelera. Zoona ndinena kwa inu, Kuti adzamupanga iye kukhala oyang'anira katundu wake. Koma ngati wantchito woipayo, adzati mumtima mwake, mbuye wanga wachedwa kubwera; ndikuyamba kumenya anzake ogwira nawo ntchito, ndikudya ndikumwa ndizidakwa, mbuye wa wantchitoyo adzafika tsiku lomwe samayembekezera kumuona, komanso panthawi yomwe samayembekezera. Ndipo adzamuchotsa, ndikumusankha kukhala mmodzi mwa amthira kuwiri: kudzakhala kulira ndikukuta mano."

AMBUYE amatipatsa zizindikiro zambiri, tsono ngati mukumvetsera, simudzadzidzimutsidwa. Awa ndi masomphenya ena omwe muyenera kuwaganizira, chifukwa masomphenya amenewa adzasandulika choonadi mwamsanga kuposa mmene mukuganizira: "Ndipo ndinaona kumwamba kutatseguka [awa ndi masomphenya ena akutha kwa nthawi kuchoka kwa MULUNGU], ndipo taonani kavalo woyera; ndipo IYE wamukhalirapoyo anatchedwa WOKHULUPILIKA ndi WOONA, ndipo m'choonadi IYE aweruza ndikuchita nkhondo. Maso AKE anali ngati Malawi a moto, ndipo pamutu PAKE panali zisoti zaufumu zambiri; ndipo IYE analembedwa dzina lomwe palibe munthu anadziwa koma IYE MWINI YEKHA. Ndipo IYE anavekedwa nsalu yoviyikidwa m'mwazi: ndipo dzina LAKE likutchedwa MAWU a MULUNGU. NDIPO ASILIKALI ANALI KUMWAMBA ANAMUTSATIRA IYE PAMAKAVALO WOYERA [amenewa ndi AMBUYE ndi atumiki AWO, alonda], atavala nsalu yosalala, yoyera ndi yosamalika. Ndipo kuchoka mkamwa MWAKE munatuluka lupanga lokuthwa, lomwe IYE adzamenyere nalo mitundu: IYE adzawalamulira ndi ndodo yachitsulo [MAWU a MULUNGU]: ndipo IYE anafinya ukali ndi mkwiyo wa MULUNGU WAMPHAMVU ZONSE. Ndipo IYE pansalu YAKE ndi pantchafu YAKE palembedwa, MFUMU YA MAFUMU, NDI AMBUYE WA AMBUYE [uyu ndi YESU AMBUYE wathu.]" (Chivumbulutso 19:11-16).

Pano tikukhala mumphindi zochepa zanthawi yotsiriza. Zizindikiro zonse zilipo. Boma la dziko limodzi lokana Khristu likugwira ntchito tsopano. Gawo lokhala mlengalenga la MULUNGU lakhala likugwira ntchito kwa zaka, ndipo anthu mahandiredi a mamiliyoni akhala akuona izi (mbale zowuluka, alonda, angelo, asilikali a okhulupirika a MULUNGU a mlengalenga). Papa ku Rome akutumbwa ndi mmene New World Order ikuchitira. Kuli tsunami, mafunde, zivomerezi, milili ya mitundu yonse, matenda, kusokonezeka kwa maiko, mazunzo ndi mahandredi a matembelero a mitundu yosiyanasiyana.

Ndinu abwino kapena oipa.[11] Mudzatha kulandira Khristu ngati MPULUMUTSI wanu, kapena kumukana IYE. Sankhani IYE tsopano, nthawi

*(Yapitirira patsamba 8)*

**11** Mat. 7:15-20, Yak 3:11-12, Chiv. 20:11-15, 21:7-8, 24-27, 22:11-12, 14-15

## Umboni wa Steven Wedel



*M'bale Steven Wedel*

Dzina langa ndine Steven Wedel. Ndinakwanitsa zaka 59 kumapeto kwa October, 2012. Ndinalandira Khristu ngati Mpulumutsi wa moyo wanga pa 4 November, 1971. Nditangokwanitsa zaka 18 mwasabata yathayo. Chikhala kuti Khristu sanalowe m'moyo mwanga mmene analowera nthawi imeneyo, bwenzi pano mutawerenga za imfa yanga zaka zapitazo, mmalo mowerenga umboni wamphamvu ya Mulungu ndikuthekera posintha moyo wa munthu omwe mukuwerenga panowu.

Pamene ndinamaliza maphunziro a sekondale nthawi ya dzinja m'chaka cha 1971, ndinalibe maganizo okapitiliza ku koleji. Ndinkadzitenga ngati odziwa zinthu. Ndinapita koyamba ku San Francisco, California, ndi anzanga ena pa galimoto, ndipo ndititatulutsa chala changa panja, kuyendetsedwa kuchoka ku San Francisco, mpaka ku Boulder, Colorado, kenako kubweranso ku California, pano ku Los Angeles.

Mayi ake amzanga amene ndimayenda naye anali ndi nyumba yaikulu kwambiri komanso yokongola ku Beverly Hills. Anatiyitana kudzakhala nawo pang'ono, mpaka titapeza ntchito ndi chipinda chosamukiramo. Nyumba yawo inali ndi dziwe lapanja losambira ndiponso inali ndi wantchito amene ankapita kukagula zonse ndikutiphikira. Chikanakhala tchuthi chopambana chosangalala, koma inali nthawi yomvetsa chisoni pa moyo wanga.

Ndinamva mumtima ngati kuti ndinali osochera kotheratu komanso opanda chiyembekezo m'moyo mwanga. Panalibe chilichonse chimene chikanachotsa kusokonezeka kosatha kumene kunali m'maganizo ndi m'moyo mwanga patanthauzo la moyo ndi cholinga. Ndinamva ngati ndakodwa m'kati mwanga. Ndinkafuna moyo watanthauzo, omwe ukanatha kuthandiza anthu ena. Ndinakhumudwa ndi mmene dziko linalili, ziphuphu, kunyanyala, zaumbanda, ndikukhetsa mwazi. Ndinkafuna kukhala m'dziko la mtendere ndipo ndinaganiza kuti hippie movement ku California ikanandipatsa yankho ya mchitidwe wotopetsawu. Ndinaganiza kuti kusuta mankhwala ozunguza bongo, kumwa LSD ndi mankhwala

*(Yapitirira patsamba 6)*

# Umboni wa Steven Wedel

*(Yachokera patsamba 5)*


ena ozunguza bongo zikanandipatsa chithunzithunzi chimene ndimafuna, kupeza chifukwa cha moyo umene ndimakhala. Sindimafuna ntchito yogwira kuyamba 9 mpaka 5 koloko, nyumba ya mpanda ndi agalu komanso amphaka, ndi tsogolo lopanda kolowera. Ndimafuna kudziwa kuti moyo cholinga chake chenicheni ndi chani. Zomwe anandichita mankhwala onse ozunguza bongo ndikungondibera maganizo anga aumunthu amene ndinatsala nawo ndikundisiya ine ndi nzeru zochepa kwambiri kuti ndichite chili chonse. Ndimaona ngati ndikupenga ndipo osakayikiranso, ndithu ndinkapengadi. Koma sindinaleredwe chonchi.

Zaka zanga zakumayambiriro ndakulira kumaiko akutsidya lanyanja. Bambo anga ankagwira ntchito ndi International YMCA ku Tokyo, Japan, ndipo mokhulupirika takhala tikupita ku tchalitchi laMulungu lilichonse kutchalitchi chopanda chipembedzo. Ndakhala ndikuphunzitsidwa kuti ndife akhristu, ndipo ndinaphunzitsidwa kukhala wachifundo, kuthandiza anthu ena. Ndinkadziwa kuti Khirisimasi ndi Pasaka ndi masiku opatulika, samakhudzana ngakhale mpang'ono pomwe ndi Santa Claus kapena Easter bunny. Ndinkakhulupirira mumzimu wanga, monga ana ambiri amachitira, kuti kuli Mlengi, Mulungu yemwe analenga zonse, kuphatikiza ine ndemwe. Ndinaphunzira kukhulupirira mwa Yesu Khristu ngati Mpulumutsi, komabe sindinkadziwa kuti Yesu kwenikweni anali ndani. Ndinalibe mphamvu m'moyo mwanga, ndinalibe nyonga zodziletsera kuchimwa, ndipo zenizeni, kuyang'ana mmbuyo, palibe mwamatchalitchi omwe ndinapitako anandiphunzitsa za tchimo kuti kwenikweni ndichani. Sindinamvepo mawu oti "kubadwanso mwatsopano mwa Mzimu" ndipo sindinachitirepo umboni wa kuitanidwa ku guwa komwe mizimu inapulumutsidwa kumatchalitchi konseko. Anali okufa mu uzimu ngati mmene ine ndinalili.

Ndinkakalowa mu grade 10 kusukulu pamene banja lathu linabwelera ku United States. Sindinkafuna kukhala wakufabe muuzimu. Anthu onse ondizungulira "ankamvetsera," "kukondweretsedwa," ndi "kusiya kuchita nawo." Ndinayamba kufufuza mayankho amafunso amkati mwanga okhudza moyo, imfa, nthawi yosatha, cholinga. Ndinawerenga mabuku pazazipembedzo zaku Far East, zipembedzo zovuta kuzimvetsa, zipembedzo za anthu aku India okhala ku Amereka, anthu ozama mu nzeru, mabuku okamba za maganizo a anthu ndi zitsanzo zolongosoka, mabuku akagwiritsidwe ka zinthu anthu ambirimbiri, zinthu zopangira limodzi, dongolo lazachuma lokonzedwa ndikuyang'aniridwa ndi mwini wake—china chilichonse chimene ndinkaganizira. Ndinawerenga Baibulo, koma panthawi imeneyi, wopanda Mzimu wa Mulungu mwaine, sindinathe kumvetsetsa. Ndinaphunzira kuyimba, zachipembedzo cha mahindu (yoga), kuyenda munkhalango, kuonetsetsa kuti ndisaponde maluwa, kufika chifupi ndi Mulungu. Palibe chomwe chimakwaniritsa kusowekera kwa mkati mwanga. Palibe chimayenda.

Sindinkadziwa nthawi imeneyo, koma tsopano ndadziwa, kuti anali Ambuye kuchita nane ndikundibweretsa kumalo komwe IYE adzachepetse kudzitukumula ndi kudzikonda kwanga kukhala kumulandire IYE ngati Mbuye ndi Mpulumutsi. Analola njira zonse kukhala zolemetsa. Akhonza osagwiritsa ntchito njira imeneyi ndi iwe, koma Iye anadziwa kuti ndi njira yokhayo yomwe ingathandize kuti nzeru zanga zibwerere. Analola kuti ndibwere ku California ndi cholinga chimenechi. Anali akundikonza, koma ndisanadziwe zimenezo.

Ku Hollywood, California, munthu sungathe kuyenda mtunda wokwana 200 feet kupita ku Hollywood Blvd. usanakumane ndi mboni zochokera ku utumiki wa Tony and Susan Alamo Christian Foundation. Anali paliponse ungapite. Nthawi zonse zomwe ndapezeka ku Hollywood, pamene ndinkafuna ntchito kapena kungopha nthawi, anali paliponse kugawa mawu a Mulungu ndi kuitanira anthu kutchalitchi chawo. Anali odzadzidwa ndi chilakolako cha Mulungu. Ndinapatsidwa umboni pa za Ambuye kangapo ndikui-









*Abale ndi Alongo a Utumiki wa Alamo kutumikira kwa mzika zachikulire ku nyumba zosamalira achikulire.*

tanidwa kubwera ku tchalitchi ngati ena onse, koma ndinkakana kuitana kwawo mobwerenzabwerenza. Ndinkadzitukumulabe ndikamva ena akundiuza za Yesu. Komabe nthawi zambiri, usiku, pamene tsiku latha ndipo ndili ndekhandekha, Ambuye amandikumbutsa zinthu zimene a Khristuwa ankandiuza m'mbuyomu, malembo amene anandionetsa mu Baibulo okhudza kutha kwa nthawi, zinthu zomwe zinkaoneka mosavutikira pali ponse, malembo okhudza moyo wosatha ndi Gehena zomwe zinandipangitsa kudabwa za zinthu. Kunjako, Satana ankandikokabe, koma Mulungu mkatimu ankandikonza.

Usana wina, Mulungu anamaliza zomwe Iye anayamba muzochitikachitikazi. Ndinkamva ngati china chake chinkachitika m'moyo mwanga koma sindinkadziwa kuti ndi chani. Ndinakapezeka pa Hollywood Boulevard kenanso tsiku limenelo, osayang'ananso za abale ndi alongo ochokera ku tchalitchi, koma mmalo mwake kuyesa kuwapewa. M'malo mwake ndinakakumanizana ndi mmodzi mwa alongo pakona ya msewu yemwe anandipatsa pepala lolemba za uzimu ndipo anandiyitana kubwera kutchalitchi usiku watsikulo. Ndinapereka chifukwa chosamveka, ndinati, "ndikaganize kaye." Mwansanga anandiyankha nati, "Ndikuyenera kukaganizira, chifukwa litha kukhala tsiku lotsiliza lomwe Mulungu angakhale nane ntchito!" Palibe chimene akananena chomwe chikanandikhudza koposa. Kungoganizira kokha kuti Mulungu Mwini Wake atha kukhala alibe nane ntchito kunandimenya kwambiri kuposa nyerwa kugendera pamaso panga. Izi zinandiopsa kwambiri. Ndinazunguzika mutu, koma osati kuzunguzika kondipangitsa kuti ndisadziwe kuti Mulungu kundisiya ndekha chikhonza kukhala chinthu chotsilizira chimene ndingafune. Izi zinandipatsa mantha. Ndinali nditakhumudwa kokwana kale.

Ndinayenda mpaka kukafika ku Hollywood Boulevard ndi mbali yansewu imene inali ndi nyumba zikuluzikulu ndi ma Yard akulu m'mbali mwake. Ndinakhala pansi pamodzi mwa ma Yard ndikudikira mpaka kufikira pafupifupi nthawi imene basi yotenga anthu kupita nawo ku tchalitchi inatsala pang'ono kunyamuka, kenako ndinapita kumene basi inkanyamula anthu ndipo ndinakhala pa mpando.

Ulendo opita ku tchalitchi ku Saugus unali wautali, koma ndinamva ngati ndili kunyumba. Mmodzi mwa abale muchiKhristu anatululutsa gitala ndipo anatsogolera anthu onse kuimba nyimbo za Mulungu mpaka kukafika. Ndinamva mtendere kwambiri ngakhale zinali zachilendo kwaine nthawi imeneyo.

Titafika kutchalitchi, alendo onse amene anabwera pa basi anaitanidwa kuti alowe ndikukhala nawo pa mapemphero. Sindinakhalepo mutchalitchi ngati ichi, chomamveka kuti n'chamoyo. Chinali chosafowoka ngati matchalitchi ena amene ndakhala ndikupita m'mbuyomu kotero kuti anatsetselekera mkati. Abale ndi alongo amenewa ankayimba nyimbo za Mulungu pa nthawiyi mokwenza. Ankakweza manja awo ndi kuyamika Ambuye. Zimaoneka ngati aliyense mu tchalitchimo usiku umenewo anapereka umboni wina wake pa zomwe Mulungu anawachitira pa moyo wawo. Ena anagwiritsapo mankhwala ozunguza bongo, ena ayi. Ena anakhalapo zigawenga; ena amachokera ku ngalande za madzi ndipo ena amachokera ku gulu la blue blood. Anthuwa anali monga mmene ine ndidakalili—Okhumudwa ndi otaika. Tsopano onse anafuula kuti Khristu ndi Mpulumutsi wawo. Sanalinso otaika, koma opezeka. M'moyo mwanga, ndinkafuna zomwe zinanenedwa mutchalitchi usiku umunewo. Ndinkafuna moyo umenewo, komabe sindinali okhutitsidwa ndi zinthu zina zambiri. Satana ankaponyabe mamiliyoni azikaiko paine mu nthawi yake yotsiliza yoyeselera kundilepheretsa kuti ndipulumutsidwe. Baibulo limati "Khulupirani mwa Ambuye Yesu Khristu ndipo mudzapulumutsidwa." Pamaitanidwe a kuguwa usiku umenewo, Satana anandisiya. Ndinakhulupilira mwa Mbuye Yesu Khristu usiku umenewo pamabondo anga kutsogolo kwa mpingo ndipo ndinapulumutsidwa! Alemekezeke Mulungu! Alemekezeke Ambuye nthawi zonse pakukhala IYE wodekha ndi chifundo chimene IYE anali nacho pa ine! Ndinabadwanso mwatsopano!

Ndinamva Ambuye atalowa mumtima mwanga usiku umenewo ndipo sindidzalola kutaya ichi. Sindidzasiya ichi kuchoka mwa ine. Kupita ku chipinda chopemphelera mapemphero atatha komanso kumadziwadi tsopano kuti kuli Mulungu Kumwamba yemwe amandisamalira ndi kuyankha mapemphero ndichinthu cha mtengo wapatali m'moyo wanga ndipo ndimasangalala kwambiri. Ananditengera ku malo usiku umenewo ndipo sindidzayiwala. Anandipatsa ubatizo wa Mzimu Woyera patapita masabata awiri. Panalibe chomwe chikananditsimikizira nditakumana ndi zimenezi kuti Mulungu siweniweni. Iye ndiwamoyo, ndipo Iye ndiwamoyo mpaka muyaya. Iye anandipulumutsa ine ndipo Iye atha kupulumutsa iwe. Ndaona anthu masauzande akutengeredwa kwa Khristu kudzera mu utumiki umenewu kuyambira nthawi imeneyo. Ndaona makamu makamu a anthu akuchiritsidwa ndi mphamvu ya Mulungu ku matenda amene anali nawo. Ndaona miyoyo ya anthu yomwe inali yotayika (ngati waine) ikusinthidwa kukhala yobereka zipatso. Sindingagulitse moyo wachi Khristuwu ndi china chilichonse chomwe dziko lingalonjeze.

Tony ndi Susan Alamo anali anthu omwe Mulungu anawagwiritsa ntchito kuti abweretse masauzande a anthu kuchoka ku mbali zonse za moyo kukapeza moyo watsopano mwa Khristu. Onse anapanga izi mosadzikonda. Sanafunsepo chilichonse kwa aliyense mwakusinthanitsa kanthu, koma kutumikira Ambuye kokha. Susan anapitilira kukakhala ndi Ambuye m'chaka cha 1982 ndipo Tony wakhala akupitilizabe kuchita za uthenga wabwino tsiku ndi tsiku kuyambira nthawi imeneyo. Iye adakapitirizabe. Ine, pamodzi ndi anthu ena, tili oyamika kwambiri kwa awiriwa osati chifukwa chokhala ndi chidwi pa Mulungu kokha mwa iwo kukhanzikitsa abale ndi alongo mmiseu kuti azifikira anthu ena ofuna thandizo tsiku ndi tsiku, komanso kupereka malo amene anthu ngati ine akhonza kukhala moyo opatulika, wa uMulungu ndipo osadzapezekanso muzochitika za dziko la uchimoli. Tiyamike Ambuye!

Ngati mukuwerenga umboni umenewu ndipo simunapulumutsidwebe, musachedwe. Yesu Khristu ndiyedi Mpulumutsi wa dziko lapansi, ndipo Iye atha kupatsa chili chonse chimene muchisowa. Iye anandipulumutsa ine, Iye anandipatsa chinthu choti nditha kukuwira, chinthu choti ndingakhalire nacho moyo komanso kuchifera. Iye atha kuchita chimodzimodzi kwa inu. Musachedwe. Mulowetseni Iye mumtima mwanu lero!

Tiyamike Ambuye,
Steven Wedel

## ASILIKALI A NKHONDO YAPAMTUNDA NDI MLENGALENGA A MULUNGU (ALONDA)

*(Yachokera patsamba 5)*

isanathe. Mwangotsala ndimpweya umodzi, kugunda kwa mtima kumodzi, kuti mufike kumoyo wosatha.[12] Mukunena pempheroli chifukwa cha mzimu wanu. Ndipo mubatizidwe, kuviyikidwa thupi lonse mmadzi, m'dzina la ATATE, la MWANA, ndila MZIMU WOYERA.[13] Phunzirani Baibulo la King James Version ndikusunga malamulo.[14] Yendani mu MZIMU wa MULUNGU.[15]

**AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.[16] Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.[17] Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wamtengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.[18] Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,[19] ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.[20] Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.[21] Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wamtengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.[22] Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.[23] MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.[24] Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mundipulumutsa.[25] Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.[26]**

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.[27] Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu,* [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.[28]

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu (Marko 16:15). Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa Mbusa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mundiyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhalenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

**12** Mlal. 3:19, Yes. 2:22 **13** Mat. 28:19-20 **14** 2 Tim. 2:15, 3:14-17 **15** Ezek. 36:27, Aro. 8:1-14, Agal. 5:16-25 **16** Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 **17** Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 **18** Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 **19** Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 **20** Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 **21** 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 **22** Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 **23** Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 **24** Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 **25** Aheb. 11:6 **26** Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 **27** Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 **28** Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

***Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.***

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**
**Twenty-four hour prayer and information line: (661) 252-5686 • Fax (661) 252-4362**
**www.alamoministries.com • info@alamoministries.com**

*Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika Kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse*

**Maservice amachitikira ku New York City lachiwiri lililonse nthawi ya 8 koloko usiku ndi malo ena usiku okhaokha. Chonde imbani (908) 937-5723 kuti mudziwe zambiri. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PAMAPETO PA MAPEMPHERO ALIWONSE.**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti *Mesiya,* losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

*Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo*
*Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira*
*Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa (661) 252-5686.*

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12). MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**

© Copyright February 2013, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo ® Registered February 2013, 2015

CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 17400—*THE ARMY AND AIR FORCE OF GOD*